03-06-14

locallangs EVE

VEEP MALAWI

Item one

Vice President GUY SCOTT has held talks with Malawi's newly elected President PETER MUTHARIKA in Blantyre.

Speaking to ZNBC at Professor MUTHARIKA'S RESIDENCE THIS MORNING, Dr SCOTT said Zambia will work with the new Malawian administration to foster development in various areas of interest.

Dr. SCOTT said it is important that trade between the two countries is made smooth.

And professor MUTHARIKA said his government is ready to boost the cordial relations that have existed between Zambia and Malawi for decades.

President MUTHARIKA said both governments must work to improve the lives of the two peoples.

Ends...BM...PIX/KB/AM

Received From SUB at 19:16 Hrs On 04062014

**E0306143**

Item 3

Government has given sichili mission hospital in Mulobezi District new laundry equipment.

Schili Mission Hospital in mulobezi District Acting Administrator PAMELA MARIA-JOS says the government is also building a new Xray unit at the hospital.

Sister PAMELA also told ZNBC news in an interview in Mulobezi that the hospital has also received a six body capacity mortuary unit.

Sister PAMELA says the government has also donated a new ambulance and sent a Zambian doctor for the first time since it was built in 1944.

She further says the hospital has already submitted a bill of quantity to the provincial administration in western Province for the construction of new wards to replace the old ones that collapsed.

**APPENDIX IV**  
**News in Nyanja**

**N1308121**

**Item one 1**

Nduns yaciwiri yachigayo coona pa nkhani mkati mwadzikoli Bambo Ngosa Simbwakula, ati anthu kutenga lamulo m’manja mwawo ngati pali zovuta.

A Dr. simbwakula ati boma lili ndi cisoni pa imfa za anthu omwe anaphedwa pa ciwawa comwe cinachitika ku chambishi, masabata awiri apita, komwe anthu anatentedwa pambuyo powaganizila kuti amachita zinthu za usatana.

Iwo analankhula izi pambuyo poyendela malo omwe panachitikila ciwawa chimenechi ku chambishi.

A Dr. Simbwakula auza atsogoleri kumaloko kuti agwile nchito pamodzi ndi apolisi pophunzitsa anthu akomweko zakuipa kwake ngati munthu waphwanya lamulo ladziko, kuti zotelezi zisakachitikenso.

**N1308122**

**Item two 2**

Kabungwe ka boma kofufuza kayamba kufufuza pakagulidwe ka mafuta pakati pa mwa ena omwe kale anali akulu-akulu mboma la MMD ndi makampani ogulitsa mafuta kudzikolo la Nigeria.

Olankhulira kabungweka, Namukolo kasumpa, atsimikiza izi ku atola nkhani a wailesi ino ya ZNBC, koma akana kufotokoza zambiri pa nkhanayi.

Kalembele muunduna wa zamagetsi ndi madzi, bamboo George Zulu, kumbuyoku anavumbula kuti boma la MMD inagula mafuta okwanila 90 metric tones ku kampani ina yace ya kudzikolo la Nigeria koma sanafike mdziko la Zambia.

**Pomaliza nkhani.....**

**N1309123**

**Item three 3**

Bungwe loona pa za msegwela la football Association of Zambia, FAZ layamba kufufuza malipoti akuti akulu-akulu ena abungweli anazembetsa maticket amasegwela omwe anachitika pakati pa dzitolo la Uganda ndi Zambia, ndikukagulitsa pa msika.

Matikiti awa anali amasegwela olimbilana kukapezekako ku mpikisano wa 2013 AFCON, pakati pa dzitolo la Zambia ndi Uganda kubwalo la masegwela la Levy

Mwanawasa ku mzinda wa Ndola, komwe anyamata achipolopolo anapambana cigoli cimodzi kwa zii.

Olankhulila bungwe la FAZ, bamboo Erick Mwanza, ati izi zinapangitsa kuti matikiti amenewa, ndipo ati aliyense yemwe adapezedwa kuti anachita izi adzapatsidwa mlandu.

#### **N0403151**

##### **Item one**

Nduna ing'ono ku ofesi ya wachiwili kwa mtsogoleri wadziko lino bamboo Stephen Kampyongo wauza ma District Commissioner kuti ayenera kuona ndi kusimikiza kuti bvuto yakuongeka kwa chimanga muminda kamba kakuchedwa kwa mvula isakhale bvuto imene izabweretsa njala mumadera awo.

Bambo kampyongo wati ofesi yao izafufuza mokwana mumwezi a April ndi mwezi wa May ndicholinga chofuna kudziwa m'mene ulimi wayendera wanyengo ino mumaboma onse ndinso mdziko lonse.

Nati maboma okwanila asanu ndi atatu (8) pa maboma khuni ndi anai (14), kudera la Western province yakuyembekezereka kukhla ndi bvuto lakuchepekera kwa chakudya kamba mvula komweko inayamba mochedwa kugwa.

Bamboo Kampyongo auzanso ma district Commissioner kuti ayenera kudziwitsa mwamsanga achigao chomwe pazotogwera mwadzidzidzi cha Disaster Management and Mitigation Unit za bvuto iliyonse imene yagwa mudera lao m'malo mothamngila kwa atola nkhanu.

Bamboo Kampyongo amalankhula zonsezi pomwe analukambilana ndi atola nkhanu muno Lusaka.

#### **N0403153**

##### **Item two**

Ndua imene ikuona pathumba landalama zadziko lino, bamboo Alexander Chikwanda wati ulimi wakula wa mbeu zosiyana-siyana zomwe zingagulisidwe kunjira kwadziko lino utha kubweretsa ndalama zambili zakunja zomwe zingathandize kukomesa mphamvu zandalama yathu kwacha.

Bamboo Chikwanda wati kupyolera ulimi dziko la Zambia litha kupezerapo ndalama zambili zochokera lino zomwe zingathandize kukomesa maziko achuma chadziko lathu.

A Chikwanda apempha nzika zadziko lino kuti zisamada nkhanu mopitilila malile ndi kugwa pansu kwa mphamvu zandalama yathu tikayekeza ndi ndalama zamaiko akunja otukuka, cifukwa kutero kutha kupangisa kuti ndalama yathu igwenso pansu.

Bamboo Chikwanda wati dzikola Zambia liyenera kuyika nzeru kwambili panchito zamalimidwe ndi nchito zokopa alendo kotero kuti tipeze njila imene ingathandiza kubweretsa ndalama zakunja.

Nati kugwa pansu kwa kwacha ndi gao la 24 percent kuchokera muchaka cha 2013, kukuonesa kwenti-kwenti m'mene maziko achuma alili mdziko muno.

Kulankhula munyumba yamalamulo a Chikwanda wati nzika zadziko lino sizambili zomwe zikutengako mbali panchito zothandiza pa kutukula maziko achuma chadziko lino.

A Chikwanda nati dziko la Zambia likugula zinthu zambili kuchokera kunja kupambana zinthu zomwe tikupanga tokha muno mwathu, nati boma mmogwilizana ndi Bank of Zambia lizapitiliza kufuna-funa njila zimene zingathandize kukomesa mphamvu za ndalama yathu kwacha.

Nasimikizila aphungu amunyumba yamalamulo kuti zinthu zizakhala bwino mukupita kwamasiku muchaka chino.

Nati chimene changisa kuti mphamvu za kwacha zibwere pansu ndi kamba kakuchuluka kwa anthu omwe akufuna kugula kapena kusinthisa ndalama ya dollar imene ikuchepa tsopano kamba kakuchuluka kwa anthu omwe akuyifuna.

A Chikwanda anatinso china chomwe chapangisa kuti mphamvu kwacha zigwe ndi kutsika kwamtengo wa mwala wakkopa pamsika.

### **N0403153**

Item three

Nduna imene ikuyanganire dera lakumawa kwadziko lino, bamboo Malozo Sichone wati anchito zachitetezo kuti asilikali mudera limeneli lakumawa, akugwila bwino nchito zao zachitetezo maka-maka mboma la Chipata pokhala kuti bomali lili kumalire adziko lino.

Kulankhula pomwe nduna ing'ono ku unduna umene ukuona panchito zachitetezo mdziko muno bamboo Christopher Mulenga anapita kukawayendera ku ofesi yao paulendo wao woyendera makampa ya asilikali komweko. Bamboo Sichone anati mboma la Chipata simunakhaleko ziwawa zirizonse zazi kulu kamba kakuti asilikali amachita zinthu mwamchangu.

Kwinaku bamboo Sichone apempha chigao cha asilikali cha Zambia National Service pa kampa ya Chikowo kuti aziphunzitsako nchito zachitetezo ku achichepere omwe akuphunzila zamalimidwe pomwepo kotero kotero kuti azikhala ozilemekeza monga asilikali aboma.

Endsjose/2015

Ends/mwale/znbc/pix

**N2202153**

Item three

Amfumu Mukobela amboma la Namwala wati chkhaliidwe chosankhana pamitundu sichifunika muno mwathu mu Zambia ndipo nzika zones zabwino zofuna zabwino mdziko lathu lino la Zambia ziyenera kugwapo panchito yogwebana ndi chikhaliidwe chimenechi choipa.

Amfumu Mukobela anati zichitidwe zilizonse zomwe zikupitisa patsogolo chikhaliidwe chimenechi choipa kuchokera ku munthu aliyense chiyenera kuzuzulidwa chifukwa ichi chitha kupangitsa kuti dziko lathu ligawanike.

Amfumuwa apempha azitsogoleri onse pamodzi ndi mfumu zinzao mumadera onse adziko lino kuti ayenera kuphunzitsa anthu awo zakuipa kwa sankho pamitundu ndikuuza anthu awo kuti ayenera kulandila munthu wamtundu uliwonse akafika mudara lao kopanda sankho, kotero kuti umodzi mdziko upite patsogolo.

Endjose/2015.

**N0303151**

Item one

Apolisi mumzinda uno wa Lusaka, anapita unkafuluza nyumba ya mtsogoleri wacipani cha United Party for National Development, UPND, ya ku new Kasama, likulu la cipani ndi nyumba yakale ya a Hichilema ku kabulonga.

Ndipo apolisi ayamba kufufuza nkhani yomwe a Hichilema ati anafalitsa uthenga wakuti iwo amalandila uthenga wacinsinsi omwe umafunika kudziwidwa ndi mtsogoleri wadziko.

Olankhulila apolisi, Charity Munganga, anatsimikiza izi ku atola nkhani a ZNBC mu uthenga.

Mai Munganga, acenjeza nchito aboma omwe adzapezeka ndi uthenga wacinsinsi waboma, kuti adzamangidwa ngati apeleka uthengawo ku anthu osayenela ku ulandila.

Ndipo atola nkhani a ZNBC ndi Daily Nation, anachitidwa cipongwe ndi acimembala a UPND ndipo anawatsekeleza kulowa mumanyumba awiri onse, ati cifukwa amakondela kufalitsa ndi kuulutsa nkhani kwawo.

### **N0303152**

Item two

Mkazi wamtsogoleri, mai Esher Lungu, adandaula ndi kucepekela kwa azimai omwe akutengako mbali ku ndondomeko za chitukuko mdzikoli.

Iwo ati mpofunika kuyambitsa ndondomeko zambiri za chitukuko zomwe zidzathandiza azimai makamaka omwe ali mbali zakumidzi.

Polankhula pomwe analankkhula ndi azimai pa Walamo Hall ku Mpulungu, mai Lungu anathookoza kuboma la Mpulungu povotela mtsogoleri Edger Lungu, pa masankho omwe anachitika pa January 20.

Mai Lungu Omwenso anakumana ndi azimai pa msika wa Ngwenya anali pamidzi ndi yemwe kale anali mkazi wamtsogoleri, Vera Chiluba Tembo, analinso ndi akazi azinduna ndi akulu-akulu acipani cha PF.

### **N2207143**

ITEM THREE

Waciwili kwa mtsogoleli wa dzikoli a dr guy scot, dzolo anakambilina ndi nduna yowona pa nkhani zakunja kwa dziko la Scotland bamboo UUMZA YOUSAF pa momweo angatheswele uphawi kumbali zaq kumbdizi

Kukambilana kumeneku kunachitikila ku msonkhano wa nduna za boma.

A DR SCOTT omwe ali mdziko la Scotland kutengako mbili mu msonkhano wa commonwealth Games Trade and BusinessConference, anatengako mbali mu msonkhano umeneu pamodzi ndi akulu – akulu a ku ofesi la kazembwewa dzikoli mdziko la England.

Ndipo bamboo Yousaf anati boma lao likuona pa momwe angasakulile fakitale yapangilapo mowa wa whisky mdzikoli la Zambia kamba kakuti mowa wa whisky wa ku dziko la Scotland ndi odiwika kwambiri pakati pa zika za dzikoli la Zambia.

### **N2407143**

ITEM THREE 24-07-14

Anthu awili anamwalila pomwepo ndipo ena asanu anabvulala pa ngozi ya pamseu pomwe galimoto yomwe anali kuyendelamo inagudubuka mu m'seu ocoka ku luwingu kupita ku kasama dzulo.

Mlankhuli wa apolisi mai charity Munganga bati ngozi imeneyi iancitika kamba kothamanga kwambili.

Mai Munganga acula maina ya anthatu omwalila kuti ndi Alex Mabila ndi Wibroad Mulenga aza zakubadwa ndi 35.

Anthatu obvulala pomwe pali dalaiva, ali mchipatala ca Kasama General Hospital.

**N2207142**

ITEM TWO 22-0714

Mboni ina yauza bwalo la milandu Magistrate muno mu lulsaka kuti ndalama zokwanila 1 hundred and 28 – thusand kwacha zinalipilidwa pofuna kuwulutsila maprogramme khumi ndi asanu ndi imodzi (16) a programme ya Stand up for Zambia ya Chanda Chimba III.

Bambo Allan Mulenga azaka zakubadwa makumi asanu (50) omwe ndi mkulu wa zacitetezo ku wailesi ya kanema ya MUVI TV, anauza bwalo la milandu dzilo kuti Chanda Chimba analipila ndalama zokwanila 8 – thousand kwacha pa programme imodzi.

Iyi ndi khani yomwe emwe kale anali nduna ya cigao ca zaofalitsa a Lieutenant General Ronnie Shikapwasha pamodzi ndi a Dr Samson Phiri ndi Chanda Chimba akuimbidwa mlandu wa chiphuphu.

Zikuganizila kuti pa masiku osadziwika koma pakati pa tsiku la 1 October ndi 31 Novermber, 2010, a Lieutenant General Shikapwasha ndi a Dr Phiri mosalabadila konse anaphwanya malamulu yokhudza kuipitsa ndzina la munthu ndi malamulo akayetsedwe ka nyumba ya wailesi ya ZNBC, polamula akulu a nyumba akulu-akulu a nyumba ya ZNBC kuti awulutse programme ya Chanda Chimba yocedwa Stand Up for Zambia, mopondeleza ufulu ndi zofuna za nyumba ya wailesi YA ZNBC.

Nkhani imeneyi izapitiliza kupitiliza kukambidwa lero pa tsiku la 22 July 2014.

**N220714**

ITEM TWO 22-07-14

Anchito za m' chipatala apehedwa kuti aziona bwino-bwino za umoyo wa main di mwana emwe wabadwa posacedwa pa akalibe kutulutsidwa m' chipatala pofuna kucepetsa imfa za pakati pa ami ndi ana.

Nduna yaing'ono ya cigao za zaumoyo a Dr Chitalu Chilufya bati madotolo omweo ayanganila zipatala ayenela kutsonglela ndi kuthundiza anamwino kuti azigwila nchito yao mwaukatswili.

A Dr Chilufya alankhula izi pa chipatala ca Senga Hill pomwe anayendela cipinda ca theater ndi X-ray zomwe zidzatsakulindwa posacedwapa.

Ndipo pa chipatala cacikulu xa m'boma la Luwingu, a Dr Chilufya anapeza mwana emwe anapsya ndi moto wagona pa bedi palibe nzofunda, ndipo iwo anauza anamwino kuti ayenela kumvelela cifundo anthu odwala.

### **N0603152**

#### ITEM ONE.

Zamveka kuti anthu atatu abanja limodzi amwalira omwe amwalira kumbuyoku muchipatala cha Kalabo District Hosipital pambuyo pakudya bowa umene unali ndi sumu kapena poizoni.

Akuti mitembo ya anthuwa kulibe munthu aliyesnse wachibale wa amene anapitako kuchipatala kuchokera panthawi yomwe anthuwa anamwalira mwezi umodzi wapiti kumbuyoku, ndipo akuti mitembo iyi yapangisa kuti chikhale chobvuta kupeza poyika mitembo ina imene ikubwera kwatsopano.

Antha atatu awa pali Pelekelo Nambo, wazakakubandwa 29, Likezo Liswaniso Jr wazaka zakubadwa 6 onse ochokera mudera lochedwa Lueti.

Ndipo ichi chapangisa kuti acouncil komweko ayike masiku khumu ndi anai (14) kuti ngati achibale sazabwera kuzatenga mitembo iyi azayika m'manda.

Amene akugwililiko udindo wau kalemba wacocouncil bambo Kenneth Sampa wasimikiza asimikiza zankhani imeneyi.

### **N0603153**

#### ITEM TWO

Zamweka kuti boma lapeleka chenjezo kuti lizagwila munthu aliyense wanchito zandale kopanda kuyangana chipani kumene achokera ngati munthuyo wapezeka kuti akuziponya muzichitidwe zoipa zomachita ziwawa.

Ndipo boma lapempha aphungu anyumba ya malamulo ocokera chipani cholamulira ndi aja ochokera muzipani zosusana ndi boma kuti aziphunzitsa anthu kufunikira kwake kopewa zichitidwa zoyipa.

Kulankhula munyumba yalamamulo, nduna imene ikuona pankhani zochitika mkati mwadziko lino bambo Davies Mwila wati membala aliyense wachipani cha ndale amene azapezeka kuti akuchita ziwawa azamangidwa kopanda kuyangana chipani cha ndale kumene iyeyo achokera.

Kwainaku bambo Mwila alengeza kuti kupima mtembo kumene madotolo adachita pa membala wachipani cha Patriotic Front Moses Simwelu amene anatemedwa ndi lupanga ndi anthu ena mumseu woipita kubwalo landeke la Kenneth Kaunda International Airport kusonyeza kuti anamwalira matenda yena osati kupandidwa.

**N0603153**

**ITEM THREE**

Zamveka kuti boma ndilokhumudwa ndi zokamba za azitsogoleri zina zandale kuzula mtsogoleri wadziko lino President Edgar Lungu kamba kuti anapatsa nchoto mboma lao aphungu ena amunyumba yamalamulo ochokera muzipani zandale zosusana ndi boma.

Munthu walankhulilako boma bamboo Chishimba Kambwili anati president Lungu ulamuliro wao ndi wofuna kupatsa mpata munthu aliyense wokhala nduna yaboma mboma ngakhale aja omwe Sali achipani cholamulira.

Bamboo Kambwili omwe panthawi imodzinso ndiwo anduna owona pazakufalitsa khani wati cymene apresident Lungu akuchita ndi kufuna kukwanilitsa zimene adalonjeza panthawi yomemeza kuti boma lao lizakhala lobweretsa umodzi mdziko.

Ndipo kulankhula ngati wakumpando wamayusi muchipani cha Patriotic Front bamboo Kambwili anati anthu omwe akulondola mtsogoleri wachipani chatsopano cha RAINBOW bamboo Winter Kabimba akhale cheru.

Bamboo kambwili anati zokamba za bamboo kabimba kususa mtsogoleri wadziko lino president Lungu ndi zopanda pache.

Endsjose/2015.

**N2002151**

Mkulu wachigao chaboma chozenga milandu kaoena kuti Director of Public Prosecution bambo Mutembo Nchito lero akuyembekezereka kuonekera pamaso pa oweruza milandu mubwalo lamilandu la Lusaka Magistrate Court.

Mkulu ameneyu akuyimbidwa milandu ingapo pomwe pali mulandu wolephera kuyendesa bwino nchito zake ndi milandu ina yambili.

Bambo Nchito ayitanidwa kubwalo lamilandu kusatila kumangala kumene adachiata amene kumbuyoku anali nduna ing'ono ku unduna umene ukuona pathumba ya ndalama zadziko lino bamboo Newton Nguni.

Malawayers oyimilako bambo Nguni bambo Kenneth Mweemba ndi bambo Makebi Zulu wasimikiza kuti kalata kapena cisamani cinatumizidwa kale kwa bambo nchito kuwaitana kubwalo lamilandu.

Oweuza milandu a Magistrate Lameck Mwale ndiwo akuyembekezereka kupeleka ciweruzo pamulandu umenewu.

## **N2002152**

### ITEM TWO

Zamveka kuti boma yaika padera ndalama yokonzera miseu pamtunda wopitililila pa 65 kilometers mudera la North Western Province.

Miseu imene ikuyembekezereka kukonzedwa ndi miseu yamu maboma aya Solwezi, Kasempa, Zambezi, Mufumbwe ndi Chavuma.

Nduna imene ikuyanganila padera la North Western province bambo Dawson Kafwaya auza atola nkhani akuno kunyumba yawilesi ya ZNBC kuti nchito iyi ikuyembekezereka kuyamba posachedwapa.

Anduna kafwaya afotokoza kuti ndalama izi zachokera ku unduna umene ukuona panchito zamacouncil ndi manyumba.

Bambo kafwaya wati mboma la Solwezi mokha miseu yokwanila pamtunda wa 20.5 kilometers izayikidwa phula.

## **N2002153**

### Item three

Mai akunyumba kwa apresident mai Esther Lungu ayamikila kwambili kampani ya Lafarge Zambia popanga kabungwe komwe cholinga chake ndikufuna kuthandiza anthau osauka m'malo okhalamo.

Kulankhula panthawi yoyambisa zinchito za kabungwe kamene kochedwa kampani ya Lafarge yaganiza kukhazikitsa kabungwe aka mudera m'mene iwo akugwilila nchito zao.

Ndipo kulankhula pamwambo umodzi- umodzi mkulu wakampani imeneyi ya Lafarge, EMMANUEL Rigus anati kampani yao iyi yopanga cementi yaika padera ndarama yokwanila Two Million Kwacha kotero kuti Kabungwe katsopano aka kayambe nchito zake zofuna kuthandiza anthu osauka mumadera osiyana-siyana.

Endsjose/2015.

## **N2602151**

### Item one

Bungwe yoziyimila payokha, yomwe ili ndi nchito yogwebana ndi umphawi, bungwe yochedwa civil society for poverty Reduction(CSPR) yapempha boma kuti ikhalenso pansi ndi eni makampani yogaya ufa akambilane kotero kuti ngati nkotheke abwenzenkonso pansi mtengo.

Wakumpando wabungwe imeneyi bamboo John lijimu wati four kwacha imene boma lidalengeza kuti yachosako kumtengo wa ufa ndi kuyamba kwabwino, koma cymene cifunika nichakuti abwezekonso pansimtengo kotero mabanja ambili azikwanisa kugula ufa umenewu

Bambo lijimu ndi ganizo yakuti boma liyenera kukhalanso pansi ndi eni makampani ogaya ufa kotero akambilance mwakuya mtengo wa ufa ubwere pansi kuposa pa 4 kwacha kotero kuti mabaja ambili akhale nao umwai wokwanisa kugulako ufa umenewu pametngo wosika.

Nati chingakhale bwino kuti mtengo wa ufa ubwezedwe mwina ndi 10 kwacha kapena 15 kwacha ichi chizathandiza kwambili kuchepesako umphawi pakati pa anthu ambili.

## **N2602152**

### **Item two**

Zamveka kuti boma lachosapo lamulo yolesa anthu kuchotsa nkhumba kudera la Southern province kupita nazo kwina.

Lamulo iyi inayidwa kusatila kubukakwa matenda yomwe yakupha nkhumba, matenda yochedwa African Swine Fever muderalo la Southern province.

Mkulu woyanganila pazamatenda aziweto muderalo, **Bambo Charles Maseka** wati nkhumba zimene zikuchosedwa kudera la **Southern province** zimapimidwa poyamba zikalibe kuloledwa kuti zipelekedwe kumadera ena adziko lino.

Bambo **Maseka** auze atola nkhanu wa **ZANIS** mboma la Choma kuti nchito yopima nkhumba ikali kuchitika ndipo akoza malo m'mene akupimila nkhumba zomwe zikupita kunja kwa **Southern**.

## **N2602153**

### **Item three**

Chipani cha **National Restoration Party (NAREP)** chapempha boma kuti ipitilize ndi nchito yokonza miseu mumalo yokhalamo ndipo nchito iyi iyenera kuchitika mumaboma onse adziko lino.

Mkulu amene akuona pazinchito zachipani chimenechi **David kapoma** wati boma ikuchita bwino kwambili panchito imeneyi yokonza miseu mumzinda uno wa Lusaka, koma chingakhale bwino kuti nchito iyi ifike mumaboma yonse monga boma la **Chingola** m'mene miseu ndi yowonongeka kotherathu.

**Bambo kapoma** wati miseu yowonongeka monga ya mboma la **Chingola** ndi mumatauni yeni ikubwezera mbuyo chitukuko mdziko.

Nati boma liyenera kuona kuti likonza miseu mumadera onse adziko lino monga m'mene akuchitila mumzinda uno wa Lusaka.

Ends/jose2015.

**N2511141**

Item one.

Zamveka kuti akulu anchito zaboma wati kwa akaidi mundende zamuno mu zambai kukubwera chiopsezo chachikulu panchito yochijiliza kufalikira kwa matenda pakati pa akaidi.

Akulu-akulu anchito zaboma ochokera ku unduna wa nchito zaumoyo, ochokera ku unduna umene ukuona pankhani zochitika mkati mwadziko lino, akulu-akulu ochokera ku unduna wa Community nkuphatikizapo aphungu amunyumba yamalamulo omwe anapita kukayendera ndende ya mumzinda uno wa Lusaka, Lusaka Central, apempha kuti payenera khala kuonjezerako ndalama zothandizila paumoyo wa akaidi kotero kutimatenda monga TB ndi HIV/AIDS yasapitilize kufalikira pakati pa akaidi mundende.

Mkulu amene anali kutsogolera gulu limeneli, Ambrose Lufuma, amene panthawi imodzinso ndiye phungu wanyumba yamalamulo woyimila constituency ya Kabompo West muchipani cha UPND, kuchepekera kwa ndalama kupangisa kuti chikhale chobvuta kugwebana ndi kufalikira kwa matenda mundende.

Bamboo Lufuma amalankhula zonsezi dzulo pambuyo poyendera ndende ya Lusaka Central ndipo keneka kunalinso msonkhano wodyesana nzeru pankhani zokhudza kukomesa umoyo wa akaidi mundende kotero kuti azikhala athanzi.

**N2511142**

Item two

Chigao chimene chili ndi nchito yowona pachitukuko m'malookhalamo, chigao chochedwa Department of Community Development, chomwe chili pansu pa unduna umene ukuona panchito zachitukuko m'malo okhalamo, umoyo wa azimai ndi ana thambi la mboma la Mpika chalandila zofunikira zones panchito zamalimidwe kotero kuti chilandilise anthu onse obvutika pamodzi ndi alimi aja ozipeleka, ndipo thandizoli lapelekedwa kupyolera munjila yaboma yothandiza alimi yochedwa Food Security Pack yanyengo yaulimi wachaka cha 2014 kukafika muchacha cha 2015.

Izi zadziwika panthawi yamsonkhana wabungwe imene ikuona panchito zamalimidwe ndi kasamalidwe kabwino kachakudya, msonkhano umene unachitikira pamaofesi wa bungwe ya imene ikuona panchito zachitukuko m'malo okhalamo mboma la Mpika.

Kalamera wamsonkhano umenewu Precious Miti adalengeza kuti zinthuzi zofunikira panchito zamalimidwe zinayamba kubwera mbomalo masabata atatu apita kumbuyoku. Kunabwera mathumba okwanila 700 yolembera 50 kilograms ya fataleza wapamwamba, ndipo mathumba yena yokwanila 700, yolembera 10 kilograms yamtedza, kayela ndi mbeu zina zosiyana-siyana zikalikupelekedwa mumadera ena.

Mai Miti wati deralo sabata lamawa, ikuyembekezera kulandila mathumba okwanila 700, yolemera 50 kilograms yafataleza wapamwamba wa urea.

### **N112141**

Item one.

Zamveka kuti azitsogoleri azipani zandale omwe anapezekako kumsonkhano umene anayitanisa abungwe imene ikuyanganila pazamasankho mdziko muno, Electoral Commisio of Zambia (ECZ) mwachidule, ndi cholinga chofuna kuti awafotokozele zofuikira kusatila panthawi yopita kukapeleka maina wao ndi kusimikizila kuti akutengako mbali, wati msonkhano unayenda bwino kwambili.

Mtsogoleri wachipani cha Patriotic Front bamboo Edger Lungu anati msonkhano uyu unali waphindu ku azitsogoleri onse azipani zandale omwe akutengako mbali pamasankho.

Bamboo Lungu anati tsopano chili ku anthu eni ake kusankha munthu amene iwo akufuna kuti akhale mtsogoleri wadziko lino la Zambia.

Mtsogoleri wachipani cha MMD bamboo Rupiah Banda wati ndi okondwa kwambili kuona kuti ulamuliro wokomera anthu onse wa democracy ukupita patsogolo muno mu Zambia malinga ndi ciwerengero cha anthu omwe awonesa chidwi chotengako mbali kuyimilila pamasankho.

### **N112142**

Item two

Nduna imene ikuyangannila chigao cha Gender, ami Inonge Wina wati unduna wao uzagwilizana ndi mabungwe yoziyimila payokha ya azimai monga bungwe ya National Women's Lobby ndi bungwe ya Women and Law thambi yakumwera kwadzikko lino la Africa kuti afune-fune ndalama ndi kusankha kenaka kuthandiza azimai omwe azayimilila pamasankho amuchaka cha 2016 osankha mtsogoleri wadziko, aphungu amunyumba yamalamulo ndi macouncillor.

Mai Wina wati azafunsaso kukambilana ndi zipani zandale kuti zikapatse mpata azimai ambili kuyimilila pamaudindo aumphungu wanyumba yamalamulo ndi ucouncillor.

Amalankhula zonsezi muno mu Lusaka dzulo pomwe analupeleka zikalata zitatatu zothandizila panchito zaboma zofuna kulinganaiza pakati pamaufulu wa azibambo ndi azimai ndikuyanganaso pamaufulu ndi chitukuko cha ana ndi azimai.

Mai Wina anafotokoza kuti ngakhale kuti posacedwapa azimai akhala akupasidwa maudindo apamwamba muzigao zaboma monga muchigao chanchito zachilungamo, muchigao cha nchito za apolisi, muchigao cholesa ziphuphu ndi chigao cha Drug Enforcement Commisiion, pakufunikila kuonjezerapo ciwerengero ca azimai mumaudindo apamwamba.

### **N1112143**

Item three

Zamveka kuti apolisi muno mu Lusaka akufufuza nkhani m'mene anthu awili omwe akukhalila pambuyo chipani cha UPND anapandidwa zolimba kamba kakuti anavala zovala zachipani cha UPND.

Munthu wolankhulilako apolisi mai Charity Munganga wati apolisi ayambe nchito yofufuza nkhani imeneyi ndicholinga chofuna kugwila anthu omwe anachita zimenezi.

Ndipo munthu wolankhulilako chipani cha UPND bamboo Cornelius Mweetwa wati ndi okhumudwa kwambili ndi zichitidwe zotere zachiwawa.

Bamboo Mweetwa wati modzi mwa mayusi dzina lake Webby Mwaba anapwetekedwa zolimba pachiwawa chimenechi chomwe chinachitikila pachiteshi cha Inter City muno mu Lusaka dzulo.

Endsjose/2014.

### **N3012141**

Item one.

Amene akugwilizila udindo wau president wadziko lino, Dr. Guy Scott wati boma ikukambilana ndi makampani yamigodi ndicholinga chofuna kupeza njila yabwino imene ingathandize kuthetsa mabvuto yomwe yalipo palipano.

A Dr. Scott kwinaku wati boma sizaopsezewa ndi akulu-akulu akampani ya mugodi ya Barrick Gold Lumwana mine omwe akupeleka chiopsezo chakuti azatseka mugodi wao pa 1 january kamba kakuti boma idakhazikitsa malamulo atsopano oyendesaramo nchito zamigodi maka-maka pankhani zokhudza misonkho imene eni migodi ayenera kulipira.

A Dr. Scott auza eni kampani imeneyi yochokera kudziko la Canada kuti adziwitse bomam'mene akuyendesera zinchito zao muno mu Zambia.

A Dr. scott amalankhula zonsezi panthawi yamsonkhano wa pamtetete kaya kuti RALLY mboma la Chililabombwe pamalo ocedwa Lubengele. Kumene adapita kukhatandizila bamboo Edger Lungu omwe akuyimilila patikiti yachipani cholamulira cha Patriotic Front.

### **N3012142**

Mkulu wina wazaka zakubadwa 41 amene ndi msozi wansomba mboma la Nchelenge wamwalira pambuyo popandidwa zolimba keneka naponyedwa mumadzi ndi akulu-akulu oyanganila pazausozi wansomba mudziko la democratic Republic of Congo.

Mkulu wa apolisi mudere la luapula province bamboo Malcom Mulenga wasimikiza zankhani imeneyi nati wophedwayo dzina lake ndi Morgan kalifungwa wochokera mudera lochedwa Mupolombo fishing camp pakachisumbu kochedwa Chisenga

Bambo Mulenga wati muthu uyu amene anali pamodzi ndi anzake ena osadziwika bwino anakumana ndi anthu anchito zaboma kuchigao chowona pazausozi wansomba mdziko la DRC, namuyimba mulandu wolephera kusatila malamulo yaboma ya pachaka yotseka mitsinje kuti nsomba zitsane.

Bambo Mulenga wati mtembo wamunthyo unapezerka tsiku losatila ukuyangalala pamadzi ndi nthawi ya 08:00 hours.

### **N3012143**

Item three

Bungwe yoziyimila payokha yochedwa Southern Center for Constructive Resolution of Disputes (SACCORD) adzudzula kwambili azitsogoleri azipani zandale zosiyana pachikhalidwe choipa chowononga maina pomwe akumemeza zamasankho yomwe tizakhala nayo mdziko muno pa 20 january yosankha mtsogoleri wadziko.

Mkulu wabungwe imeneyi bamboo Boniface Chembe iwo wati kuononga maina ya anthu ena panthawi yomemeza zamsankho ndi chintu choipa chimene munthu aliyense amene ndi nzika yabwino yadziko lino la Zambia liyenera kudzudzula.

Kwinaku bamboo Chembe apempha azitsogoleri azipani zandale zomwe zikutengako mbali pamasankho aya kuti pomwe zikumemeza zamasankho zisamanamiza anthu pomwe zikulonjeza zinthu zoisyana-siyana. Nati ndi bwino kuti zizikamba zinthu zoono.

Endsjose/2014.

### **N2801151**

Item one.

Mtsogoleri wadziko lino president EDGAR CHAGWA LUNGU wauza apolisi kuti agwepo mwamsanga kuthetsa ziwawa zimene zapitiliza mumadera ena adziko lino pambuyo pamasankho achibweleza yosankha mtsogoleri wadziko yomwe tinali nayo posachedwapa.

APRESIDENT LUNGU auza asilikali kuti achite zones zotheka kuthetsa ziwawa zimenezi maka-maka pakati pa mamembala achipani cholamulira cha Patriotic Front ndi mamembala achipani chosusana ndi boma cha UPND.

ALUNGU apempha zipani zandale zomwe zinagonja pamasankho kuti ziyenera kuvomera zotulukamo mumasankho amenewa ndi kupitiliza ndi nchito zao.

Apresident LUNGU amalankhula zonsezi kunyumba yaboma ya state house pomwe analulumbilisa phungu wanyumba yalamulo woyimilako constituency ya MONGU CENTRAL bambo NATHANIEL MUBUKWANU paudindo waunduna yoyanganila dera lakumwera kwadziko lino kapena kuti SOUTHERN PROVINCE.

Apresident analumbilisano bambo HIBENE MWIINGA kukhala mpangili wakunyumba yaboma ya state house panchito zachuma ndi chitkuko, ndinso MAI SYLVIA CHALIKOSA amene alumbilisidwa kukhala kazembe woyimila dziko la ZAMBIA kudiko la NAMIBIA.

### **N2801152**

Item two

Zipani zandale zosiyana-siyana zathokoza kwambili mtsogoleri wadziko lino EDGAR LUNGU pakuvomekeza ndi kusaina kuti bambo Henry Kanyanta Sosala akhale paudindo wa mfumu yaikulu ya anthu amtundu wa chibemba kapena kuti PARAMOUNT CHIEF CHITIMUKULU.

Wakumpando wachipani cha National Restoration bambo FRANK SICHONE wati zimene achita apresident Lungu achita kulingana ndi lonjezo yao panthawi analikumemeza zamasankho.

Kuza muthu woluzanisa zinchito cha UNITED PARTY FOR NATIONAL DEVELOPMENT bambo BATUKE IMENDA a LUNGU achite bwino koma zimenezi zimayenera kuchitika kale ngako.

Iwo wati anthu amtundu wa chibemba kupyolera munduna zao zochedwa BASHILUBEMBA sanalakwe kusankha bambo Sosala kuti ndiwo atenge udindo wa mfumu yao yaikulu CHITIMUKULU.

### **N2801153**

Item three

Chipani chosusana ndi boma cha UNITED PARTY FOR NATIONAL DEVELOPMENT chapempha nzika zadziko lino la Zambia kuti ziyenera kuona kuti mdziko muno mugwilizana, mtendere ndi bata zikupita patsogolo.

Wakumpando wachipani cha UPND mai MUTALE NALUMANGO wati kutulusa mau yonyoza kapena kuopsezana, zichitidwe zotere zitha kubweresa mikangano ndi kugawanikana kwa dziko.

Mai Nalumango wati chiopani cha UPND chikufuna kuona kuti mugwilizano ndi mtendere zikupitiliza mdziko muno.

Mai Nalumango amalankhula zonsezi muuthenga wao umene atumiza kuno kunyumba yawailesi ya ZNBC lero.

Nati mamembala achipani cha UPND azasatila zimene adakamba mtsogoleri wao bamboo HAKAINDE HICHILEMA kuti akufuna bata, mtebndere ndi mugwilizano kupitiliza muno mu Zambia pakati pa nzika zadziko liko.

Ends.

**N0802151**

**Item one.**

Zamveka kuti boma sizakhala kupenyerele anthu aulesi panchito maka-maka muzigao zaboma aja omwe akufuna kubweza chitukuko chanchito zaboma kumbuyo.

Nduna imene ikuyanganila dera lakumpoto komanso kumadzulo pang'ono kwadziko lino, bamboo Dawson Kafwaya wati mtsogoeri wadziko lino president Edgar Lungu ndi munthu wozipeleka panchito ndipo akufuna kupeleka chitukuko mumbali zones lino la Zambia.

Bamboo Kafwaya anati ndi chinthu chokhumudwisa kwambili kuti anthu ena ogwila nchito mboma maka-maka kuderalo la North Western Province omwe akuchita mwadala kusaika nzeru panchito ndicholinga chofuna kusokoneza nchito zachitukuko zimene boma likugwila.

Anduna Kafwaya imwe ali paulendo woyenderalo la North Western ndicholinga chofuna kuona m'mene nchito zachitukuko zikuyendera komweko. Iwo amalankhula zonsezi mboma la kasempa dzulo pomwe anapita kukayendera district commissioner wabomalo bamboo Victor Kayekesi.

Nati apresident Lungu ndi mtsogoleri amene akufuna kuona kuti mdziko mukhala mugwilizano anthu akukhala omvana ndikupasa mpata munthu aliyense ndi nzika ladziko lino kopanda kuyangana chipani chimene akukhalila pambuyo kuti asewenzele dziko lake.

Kwinaku, bamboo kayekesi anapeleka mafuno kwamtsogoleri wadziko lino bamboo Lungu posankha bamboo Kafwaya ochokera muchipani cha UPND kuti akhale nduna yoyanganila deralo la North estern province, nati kutero ndikubweretsa mugwilizano mdziko.

## **N0802152**

Item two

Wachwili kwamkulu oyanganila zinchito za apolisi kapena kuti Deputy Inspector General of Police bamboo kakoma kanganja asimikizila nzika zadziko lino kuti iwo azagwila nchito mwamphamvu ndiponso mozipeleka pofuna kuona kuti apolisi akugwila nchito zao mwaukastwili ndiponso mosatila malamulo adziko nthawi zones pomwe ali panchito.

Bamboo kanganja wati apresident Edgar Lungu anawauza kuti ayenera kuona kuti apolisi akugwila nchito mofikapo ndiponso mogwilizana kotero kuti dzina labwino lachigao cha apolisi lipite patsogolo.

Iwo anauza atola nkhani akuno kunyumba yawailesi ya ZNBC azafuna kuona akugwilizana ndi kusewenzela limodzi ndi mkulu wa nchito za apolisi pofuna kuthetsa dzina loyipa lachiphuphu limene apolisi akhala akudziika nalo kwa nthawi yaitali.

Nati nchito ya apolisi ndi kuona kuti bata mtendere mdziko zihupita patsogolo ndipo azafuna kugwila nchito mwamphamvu pofuna kuona kuti akwanilisa zimenezi.

Kwinaku bamboo kanganja athokoza mtsogoleri wadziko lino apresident Edgar Lungu powasankha pa udinso umenwwu wa wachiwili kamkulu wa apolisi.

## **N0802153**

ITEM THREE

Zamveka kuti nkhumba zambiali zapitiliza kufa kumatenda yachigodola chakhmunba yochedwa African Swine Fever mboma la Solwezi kudera lakumpoto komaso kumadzulo pang'ono kwadziko lino.

Ndipo izi zachitika pambuyo pamwezi umodzi kuchokera pomwe nkhumba zina zoposa pa makhumi awili zinafa mudara limeneli.

Mkhumba zisanu ndi ziwili seven ndizo zafa kale pamene zina zokwanila twenty two papulazi yochedwa BB farms mudara lochedwa mitukutuku zaphedwa ndi achigao chowona pazaumoyo waziweto komweko kuchitila kuti matenda aya yasafikile kwina.

Atola nkhani wachigao cha NAIS wati gulu akatswili owona pazamatenda aziweto komweko wasimikiza zankhani imeneyi.

Ends/jose2015.

## **N1202151**

Item One

Mtsogoleri wadziko lino president edger lungu lero walengaza maine ya nduna zaboma zomwe azigwila nazo nchito mboma lake. Apresident lungu auza nduna zaboma zimenezi zatsopano kuti ziyenera kugwila nchito mwamphamvu ndiponso mozilemekeza.

Apresident Lungu auzanso nduna zao kuti azafuna kuona kuti nduna iliyonse yaboma ikugwila nchito mwamphamvu ndiponso mozipeleka kotero kuti boma lao likwanilise zimene lidalonjeza anthu panthaawi yomemeza zamasankho.

Apresident Lungu wati udindo wa nduna yaboma yowoma panchito zachitetezo kapena kuti defense sazaikapo munthu palipano undunawu uzakhala m'manja mwao kwaka nthawi.

Ndipo asankhanso nduna ziwili zaboma kuchokera muchipani cha MMD, pomwe pali bamboo Vincent Mwale omwe ndi phungu wanyumba yamalamulo muconstituency ya Chipangali ndi bamboo Micheal Kaingu phungu wanyumba yamalamulo woyimila dera la Mwandi.

A Dr. Kaingu ndiwo apasidwe udindo wa nduna yowona panchito zamaphunzilo, kuza bamboo Vincent Mwale iwo apasidwe udindo wowona panchito za achinyamata ndi nchito zamasewela.

Apresident Lungu asankhaso phungu wanyumba yamalamulo woyimila constituency ya kabwata bamboo Given Lubinda kukhala nduns yaboma yowona pachito zamalimidwe ndi ziweto.

Amene kumbuyoku anali nduna yoboma yowona panchito za achinyamata ndi nchito zamasewela bamboo Chishimba Kambwili iwo asankhidwa kukhala nduna yaboma yowona panchito zofalitsa.

## **N1202152**

### **ITEM TWO**

Mtsogoleri wachipani cha Fourth Revolution bamboo Eric Chanda apempha nduna yaboma yatsopano yowona pazofalitsa bamboo Chishimba Kambwili kuti ayenera kuona ndi kusimikiza kuti nyumba zawailesi zaboma zikupatsa mpata zandale ndinso mabungwe yosiyana-siyana kulankhula pawailles kapena kuonekerako pawailles kanema.

Bamboo Chanda muuthenga wao umene atumiza kuno kunyumba yawailes ya ZNBC, wati bamboo Kambwili ayenera kuona kuti nzika zadziko lino zikupatsizwa mapta kapena ufulu wolankhula zakukhosi kwao pazaulamuliro wadziko lino.

A Chanda auzanso nduna yaboma yowona panchito zamalimidwe bamboo Given Lubinda kuti ayenera kuona kuti alimi akulandila zofunikira panchito yao.

A Chanda apemphanso nduna yaboma yowona panchito zamigodi bamboo Christopher Yaluma kuti ayenera kuona kuti nzika zadziko lino la Zambia nazonso zikupezerapo phindu paminyala imene ikukumbidwa muno mu Zambia pakhazikitsa misonkho yabwino imene izakondwelesa aliyense.

### **N12022153**

#### **ITEM THREE**

Mbala ina yovutisa Kwambili, imene ili ndi milandu yankhani-nkhani yosiyana-siyana yathawa m'manja mwapolisi muchitolokoso mboma la mafinga.

Mkulu wa apolisi mboma mudera la Muchinga Auxinsio Daka wasimikiza zankhani imeneyi nati mbala iyi imene inali kuyenda ndimfutim'manja ndiyo inaba mufti zitatu kudzikolo la Malawi.

Mkulu wa apolisi ku Muchinga wati dzina la mbala imeneyi ndi Dickson Singongo wochokera mboma la Mafinga ndipo anathawa muchitolokoso dzulo ndi nthawi za mawa.

Nati Singongo akuyimbidwa mulandu wakuba kugwilitsa nchito mufti ndipo amayembekezereka kuonekera pamaso pa oweruza milandu bamboo John Phiri dzulo.

Endsjose/2015.

### **N1803151**

#### **Item One**

Zamveka kuti boma ndilozipeleka panchito yofuna kumanga manyumba ya azitsogoleri akale adziko lino.

Nduna imene ikuona panchito zamtokoma, nchito zoboma ndi katundu waboma bamboo Richwell siamunene kulakhula munyumba yamalamulo, pomwe anali kuyankha funso kuchokera kwa phungu wnyumba yamalamulo woyimila Constituency ya Solwezi West bamboo Humphrey Mwaanza omwe anali kufuna kudziwa pomwe yafika nchito iyi yomanga manyumba ya azitsogoleri akale.

Bamboo siamunene wati boma palipano yapeza kale malo ku Lilayi, ku Silverest ndi ku State lodge ndipo nchito mumadera amenewa yomanga munyumba ya azitsogoleri akale yayambika kale, monga manyumba ya malemu Frederick Chuluba, malemu Lvy Mwanawasa ndi bamboo Rupiah Banda

### **N1803152**

#### **ITEM TWO**

Zamveka kuti dzulo gulu la anthu olanda katundu malamulo kulinga ndi chiweruzo cha khoti, ocedwa ma Bailiffs, analanda katundu pa likulu la maofesi azambia National Commercial Bank (ZANACO) muno mu Lusaka.

Ma bailiffs amenewa anachita zimenezi kusatila chiweruzo cha khoti yaikulu ya Supreme m'mene abanki ya ZANACO anali ndi mulandu ndi mbali ina imene inapita kumangala kubwalo lamilandu.

Mkulu wolankhulilako banki ya ZANACO mai Joy Sata wati palipano Bnaki yao nayonso yapita kukamagala kubwalo lamilandu kotero kuti mulandu uyu ayambe auyimisa pakhale kufufuza bwino poyamba.

Mai Sata palipano akupempha makasitoma abanki imeneyi ya ZANACO kuti aside nthawi ai, banki yao ikali kugwila nchito zake monga mwanthawi zones.

### **N1803153**

#### **ITEM THREE**

Zamveka kuti boma yaika padera ndalama yoposa pa 650 million kwacha yakuti akonzele masukulu amaphunzilo akuya kaya kuti Ma University.

Kulankhula munyumba yalamamulo dzulo, nduna imene ikuona panchito zamaphunzilo mdziko muno aDr. Michael Kaingu anati boma ikumanganso masukulu amaphunzilo akuya okwanila asanu.

Pomwe pali King Lewanika University mboma la Mongu, Luapula University mboma la Mansa, Solwezi University College of Science and Technology, Nalolo University College of Science and Mathematics, ndi Petauke University College of Applied Arts.

Nati boma ikufuna ukuzilakopalabana University muno mu Lusaka ndi kumanga Paul Mushindo ndinso Robert Kapasa Makasa University la Muchinga province

Endsjose/2015.

### **N2603151**

#### **Item One**

Nduna ing'ono ku unduna umene ukuona panchito zaumoyo mdziko muno, adr. CHITALU CHILUFYA alengeza kuti boma lakwanisa kale zones zofunikira panchito yomanga zipatala zing'ono-zing'ono zokwanila 650 mumadera osiyana-siyana adziko lino.

A Dr. Chiluya alengeza kuti zipatala zing'ono zokwanila 178 pa zipatala izi, zamangidwa kale palipano mumadera ena.

Iwo auza atola nkhani akuno kunyumba yawailablesi ya ZNBC kuti zipangizo zina zofunikira panchito yomanga zipatala zokwanila 155 zafika kale palipano muno mu Zambia.

A Dr. Chilufya afotozoza kuti nchito yonse izayambika posachedwapa kotero kuti nchito iyi ifike kumapeto mwamsanga.

A Dr. Chilufya wati ali nacho chiyembekezo chakuti zipatala zones zokwani 650, pazafika mumwezi wa April chaka chamawa cha 2016 zizamalizidwa.

## **N2603152**

### ITEM TWO

Kalembera mkulu wadera la Luapula province, bambo BONIFACE CHIMBWALI, wapempha anthu ogwila nchito mboma komweko kapena kuti ma civil servants kuti ayenera ugwila nchito zao molimbika kulingana ndi cholinga chaboma.

Bamboo Chimbwali amalankhula zonsezi pomwe analukambilana ndi anthu ogwila nchito mboma pamsonkhano umene anali nawo mboma la NCHELENGE pamaofesi acouncil.

Nati ndi nchito ya munthu aliyense wogwila nchito kuona kuti akukwanilisa mfundo zaboma pomwe akugwila nchito.

Kwinaku mkulu amene akuyanganira panchito zamaphunzilo mboma la NCHELENGE bamboo JONES MWENYA anapeleka dandaulo pabvuto yakusowa kwa sukulu muderalo **pochitila** maphunzilo ya nchito za 'manja za achichepere kapena kuti mayusi.

## **N2603153**

### ITEM THREE

Zamveka kuti boma lapeleka chiopsezo kuti lizakakamizidwa kutumiza kwao anthu thawa nkhondo kudziko la RWANDA kapena kuti ma refugee ngati anthuwa sakufuna kutenga zitupa zamapassport.

Nduna ing'ono ku unduna umene ukuona pa nkhani zochitika mkati mwadziko lino bembo PANJI KAUNDA wati chigao chamwathu muno mu ZAMBIA chimene chili ndi nchito yowona pa anthu olowa ndi kutuluka mkati mwadziko lino cha "IMMIGRATION DEPARTMENT", malamulo yake yaa kukambilathu poyera kuti kulibe munthu wakunja amene angakhale mdziko muno kopanda cilolezo ca malamulo adziko lino.

A Colonel Kaunda wati nzika zadziko la RWANDA za pa kampa ya MAHEBA ndi kampa ya MAYUKWAYUKWA ziyenera kuona kuti zikutenga zitupa zamapassport

zimene maiko wao akupeleka, cifukwa ngati sizizatero dziko la Zambia lizazitumiza kwao.

Mtola nkhani wathu wakuno kunyumba yawailesi ya ZNBC LILLIAN KALABA wati nduna ing'ono ku unduna umene ukuona pankhani zochitika makti mwadziko lino amalankhula zonsezi pathawi yotseka msokhano wamasiku awili wamaiko a Rwanda ndi Zambia ndi bungwe ya UNITED NATIONS HIGH COMMISSIONER FOR REFUGEES (UNHCR) mumzinda wa Kigali mdziko la Rwanda.

Endsjose/2015.

### **N1112141**

#### **ITEM ONE.**

Zamveka kuti azitsogoleri zandale omwe anapezekako kumsonkano umene anayitanisa abungwe imene ikuyanganila pazamasankho mdziko muno, Electoral Commission of Zambia (ECZ) mwachidule, ndi cholinga chofuna kuti awafotokozele zofunikira kusatila pathawi yopita kukapeleka maina wao ndi kusimikizila kuti akutengako mbali, wati msonkhano unayenda bwino kwambili.

Mtsogoleri wachipani cha Patriotic Front bambo Edgar Lungu anati msonkhsno uyu unali waphindu ku azitsogoleri onse azipani zandale omwe akutengako mbali pamasankho.

Bambo Lungu anati tsopano chili ku anthu eni ake kusankha munthu amene iwo akufuna kuti akhale mtsogoleri wadziko lino la Zambia.

Mtsogoleri wachipani cha MMD bambo Rupiah Banda wati ndi okondwa kwambili kuona kuti ulamuliro wokomera anthu onse wa democracy ukupita patsogolo muno mu Zambia malinga ndi ciwerengero cha anthu omwe awonesa chidwi chotengako mbali kuyimilila pamasankho.

### **N1112142**

#### **ITEM TWO**

Nduna imene ikuyanganila chigao cha Gender, mai Inonge Wina wati undana wao uzagwilizana ndi mabungwe yoziyimila payokha ya azimai monga bungwe ya National Women's Lobby ndi bungwe ya Women and Law thambi yakhumwera kwadziko lino la Africa kuti afune-fune ndalama ndi kusankha kenaka kuthandiza azimai omwe aziyimilila pamasankho amuchaka cha 2016 osankha mtsogoleri wadziko, aphungu amunyumba yamalamulo ndi macouncillor.

Mai Wina wati azafunanso kukambilana ndi zipani zandale kuti zikapatse mpata azimai ambili kuyimilila pamaudindo aumphungu wanyumba yamalamulo ndi ucouncillo.

Amalankhula zonsezi muno mu Lusaka dzulo pomwe analupeleka zikalata zitatu zothandizila pznchito zaboma zofuna kulinganiza pakati pamaufulu wa uzibambo ndi azimai ndikuyangananso pamaufulu ndi chitukuko cha ana ndi azimai.

Mai Wina anafotokoza kuti ngakhale kuti posacedwapa azimai akhala akupasidwa maudindo apamwamba muzigao zaboma monga muchigao chanchito zachilungamo, muchigao cha nchito za apolisi, muchigao cholesa ziphuphu ndi chigao cha Drug Rnforcement Commission, pakufunikila kuonjezerapo ciwerengero ca azimai mumaudindo apamwamba.

### **N1112143**

#### **ITEM THREE**

Zamveka kuti apolisi muno mu Lusaka akufufuza nkhani m'mene anthu awili omwe akukhalila pambuyo chipani cha UPND anapandidwa zolimba kamba kakuti anavala zovala zachipani cha UPND.

Munthu wolankhulilako apolisi mai Charity Munganga wati apolisi ayambe nchito yofufuza nkhani imeneyi ndicholinga chofuna kugwila anthu omwe anachita zimenezi.

Ndipo munthu wolankhulilako chipani cha UPND bamboo Cornelius Mweetwa wati ndi okhumudwa kwambili ndi zichitidwe zotere zachiwawa.

Bamboo Mweetwa wati modzi mwa mayusi dzina lake Webby Mwaba anapwetekedwa zolimba pachiwawa chimenechi chomwe chinachitikila pachiteshi cha InterCity muno mu Lusaka dzulo.

Endsjose/2014.

Item three

Boma lathokoza zigawo za asilikali pogwila nchito yawo mwaukatswili mdzikoli.

Waciwiri kwa mkulu wa chigawo cachitetezo ca dziko, Christopher Mulenga, ati asilikali anagwila nchito yawo mwaukatswili pa nthawi ya masankho omwe anachitika pa January 20.

Polankula ndi asilikali pa Gondar Barracks, mboma la Chipata, a Mulenga ati boma idzayamba nchito yazomanga-manga mumakamba a asilikali dziko lonse.

A Mulenga ali kum mawa kuyendela makamba a asilikali .

Ndipo a Mulenga athokoza asilikali pa kamba la Zambia Nationaal Service la Chiwoko, pokolola cimanga cambiri.

Ndipo mkulu mkulu wa asilikali a Zambia National Service, kum'mawa, Lt Colnel Jephon Kukanda, ati kamba lomwe lakhala lilikuphunzitsa achinyamata maluso osiyana-siyana ndilokonza kuyamba kuphunzitsa achinyamata ena atsopano.

Item one

Waciwiri kwa mtsogoleri wadzikoli, Guy Scitt anachita msokhano ndi mtsogoleri yemwe wangosankhidwa mdziko la Malawi, Peter Mutharika ku Blantyre.

Kulankhula ndi atola nkhani a ZNBC pa nyumba ya a Proffessor, Mutharika Lero m'mawa, a Dr. Scott ati dziko la Zambia lidzagwila nchito pamodzi ndi boma latsopano la Malawi kuti apititse patsogolo chitukuko pakati pa maiko awiriwa.

A Dr. Scott ndi chinthu cofunika kwambiri kuti zamalonda pakati pa maiko awiriwa zipite patsogolo.

Ndipo a Proffessor Mutharika ati boma lawo ndilokonzeka kukhuwimitsa ubale pakati pa maiko awiriwa.

Iwo ati maiko onse awiriwa afunika kugwila nchito zotukula umoyo wa anthu.

**N0306143**

Item Three

Boma lapeleka makina atsopano ochapila pa chipatala cha sichili mission kuboma la mulobezi

Mkulu ogwilizila Pamela Maria-Jos ati boma likumanganso cipinda ca X-ray pachipatala cimenezi

Mai Pamela auza atola nkhani a ZNBC kuti chipatala calandilanso maiosungila anthu akufa musaini, momwe mudzayamba kulowa anthu asanu ndi mmodzi.

Iwo ati boma lapeleka galimoto lonyamulila odwala, kaya kuti ambulance ku chipata ichi komanso dotolo yemwe ndi oyamba kutumizidwa kucokela mcaka ca 1944 pomwe chipatala ichi cinamangidwa.

Iwo ati chipatala capeleka kale ndondomeko ya zomwe zifunika ku akulu-akulu aboma kuti amange zipinda zatsopano mogona odwala.